



**REPUBLIC OF MALAWI**

**SPEECH**

**BY**

**HIS EXCELLENCY**

**DR LAZARUS MCCARTHY CHAKWERA**

**PRESIDENT OF THE REPUBLIC OF MALAWI**

**ON THE 60<sup>TH</sup> ANNIVERSARY OF  
MALAWI'S INDEPENDENCE DAY**

**BINGU INTERNATIONAL CONVENTION CENTRE**

**LILONGWE, MALAWI**

**SATURDAY, 6<sup>TH</sup> JULY 2024**

**Amayi ndi Abambo,**

M'mwezi wa February, ndinapita ku Nyumba ya Malamulo kukapereka ripoti kwa aphungu anu mmene dziko likuyendera, ndipo mu ripotimo ndinatchulamo zoti chaka chino tizakhala ndi chisangalalo chachikulu pokumbukira kuti dziko lathu lakwanitsa zaka 60 liri pa ufulu, pachizungu amati Diamond Jubilee. Ndipo ntangonena zimenezi, tinayambiratu kukambirana za mmene chisangalalocho chizayendere, chifukwa ma plani anali oti tidzasonkhane ku Bingu National Stadium, komanso Pulezidenti wa dziko lina amene tinkafuna adzakhale mlendo wathu wapadela tsiku limeneli tinamuitana kale ndipo anavomela kale.

Koma lero ma plani onseo takhansula chifukwa nzachidziwikire kuti ma plani omwe tinaika mu nthawi yakusadziwa sangagwire pa nthawi ino yomwe tiri mkati mwa chisoni chifukwa cha ngozi ndi imfa zowawa zomwe zatigwera mwadzidzi mwezi omwe wangothau. Komabe umu ndi mmene moyo umakhalira, chifukwa olo titapanga ma plani amtundu wanji, zomwe wakonza Chauta mawa sitimazidziwa, komanso mphamvu yomwe

**Mulungu ali nayo yosintha nyengo za miyoyo yathu ndi mphamvu yoopsywa kwambiri yomwe ikatifikira timafunika kuzichepetsa pa maso pake. Ndichifukwa chake lero tinachiona cha mzeru kuti tizichepetse pa maso pa Mulungu amene wationetsa kuti ndiye mwini miyoyo yathu, kuti iye ndiye mwini dziko, kuti iye ndiye mwini nthawi.**

**Ndiye ine ndimati ndikuthokozeni inu nonse amene mwatenga nawo gawo pa mapemphero alero, komanso inu atsogoleri amipingo ndi zipembedzo potithandiza kudzikhuthula pa maso pa Yehovah. Zomwe zachitika mdziko muno mwezi wa Juniwu ndi zinthu zoimitsa mutu kwambiri. Ndipo mpake kuti dzanali a Secretary General a chipani cha UTM, olemekezekwa a Patricia Kaliati, ananena kuti June ameneyu kunakakhala kotheka tikanakonda kuti Mulungu amufufute pa kalenda ya chaka chino chifukwa udzakhala mwezi opweteka kwambiri mu mbiri ya dziko lino mpaka kale kale. Ndiye ine kwanga nkungopitiriza kumpempha Mulungu kuti apitirize kutitonhoza tonse pamene tikuuzilirana mabala athu.**

**Ntchito youzilirana mabala ngati amenewa ndiyaikuru komanso ndiyatonse.** Ntchito youzilira mabalawa ndiyainu atsogoleri achipembedzo, chifukwa popanda mauthenga anu achiyembekezo ndi mapemphero omulirira Mulungu, tikhoza kusochera ndikuyamba kumunyozanso Mulungu yemwe ali mtonthozi wathu. Ntchito youzilira mabalawa ndi yaife am'boma chifukwa mipando yomwe anatipatsa a Malawi anatipatsa kuti tiwatumikire pachepetsa zowawa zao osati kuti tiwalamule pochita zinthu mowasungula zifukwa. Ntchito youzilira mabalawa ndiyainu atsogoleri a zipani zosiyanasiyana, chifukwa imfa ndi chinthu chowawa ndikale, ndipo imfa siimasakanizika ndi ndale popanda kuonjezela ululu wina omwe tikanatha kuupewa. Ntchito youzilira mabalawa ndi ya inu amene mwapanga kafukufuku wa ngozi yomwe inachitikayi, makamaka aja achipatala omwe anamaliza kuunikila mitembo onse ya aja anafa pangozi ija tisanawaike mmanda ndicholinga choti adziwe kuti anafa motani, komanso aja akatswiri andege akudziko la Germany omwe anamaliza kuunikila malo angoziyo ndicholinga choti adziwe kuti vuto linagwetsa ndege lina chani, chifukwa popanda kudziwitsa dziko zotsatira zakafukufuku muwiri

ameneyu, anthu apitilira kusowa mayankho amene amathandiza kuti mabala ayambe kupola. Komanso mundilole ndinene pokumbutsana kuti ntchito youzilira mabalawa ndiyainunso apolisi, chifukwa nzachidziwikire kuti pa nthawi yowawa sipalephera kupeze ka awiri atatu ofuna kuchita ziwawa mosasunga lamulo, koma inuyo monga anthu oteteza ufulu ndi mtendere wadziko muyenera kuyesetsa kugwiritsa ntchito njira zonse zowathandiza anthu kusunga malamulo musanayambe kuwamanga. Ndiye chonde mokudandaulirani, popeza malamulo samandipatsa mphamvu yokulamulani, ndimati ndikupempheni inu a Inspector General kuti muonetsetse kuti Malawi Police Service izigwira ntchito ngati Service yotumikiradi osati ngati ndi Malawi Police Force yopwetekera anthu. Koma kwakukulu, ntchito youzilira mabalawa ndi ya ife mzika zonse, chifukwa ndife amodzi komanso ululu wa imfa ndi ululu osathawika ndi munthu wina aliyense, ndiye tiyenera kumakumbukira kuti amene wamtonthoza lero azakutonthoza mawa, chifukwa imfayi ndimoto omwe omapita kumene kwatsala tchire.

**Chachikulu pamene takwanitsa zaka 60 ndikugwirizana zochita kuti tsogolo ladziko lino likhaledi labwino ndi lowala kuposa kale malingana ndi masomphenya a malemu Dr. Saulos Klaus Chilima. Chachikulu pamene takwanitsa zaka 60 ndikugwirizana kusintha kachitidwe kazinthu mdziko muno kuti mavuto omwe takhala tikulimbana nawo zaka zonsezi akhale mbiri yakale. Chachikulu pamene takwanitsa zaka 60 ndikuvomereza mbali zomwe sitinachite bwino nkuzipereka mwatsopano kuntchito yokonza monsemo poonetsa kuti tatengerapo phunziro pazinthu zowawa zomwe tadutsamo. Chachikulu pamene takwanitsa zaka 60 ndikukanitsitsa mfundo za yense amene akufuna tizingokhala bize ndindale zomenyana ndikunyozana chifukwa ndale zimenezo nzosatukula dziko komanso nzoonga tsogolo la a Malawi. Chachikulu pamene takwanitsa zaka 60 ndikutsatira chitsanzo cha malemu Dr. Saulos Chilima pozipereka kuntchito yotumikira mbendera ya dziko lino mpaka nafe tidzayifere mbendera imeneyi.**

**Ndiye patsiku la lero ine ndikudzipereka mwatsopano kuntchito yokutumikirani. Ndikudzipereka mwatsopano**

**kuntchito yotukula dziko lathu. Ndikudzipereka mwatsopano kuntchito yoyanjana ndi a Malawi onse kuti tigwire ntchito limodzi. Ndikudzipereka mwatsopano kuntchito yokweza mbendera yathu kuti miyoyo ya a Malawi nonse ikwere kuposa zipani, ikwere kuposa ndale, komanso ikwere kuposa mabala omwe tiri nawo.**

**Ambuye Akudalitseni Nonse.**

**Zikomo.**